funa Ine; ndipo [a] monga ndinanena
kwa Ayuda, kuti kumene ndinka-
ko Ine, inu simungathe kudza, mo-
mwemo ndinena kwa inu tsopano.
34 [d] Ndikupatsani inu lamulo latso-
pano, kuti mukondane wina ndi
mnzace; monga ndakonda inu, kuti
inunso mukondane wina ndi mnzace.
35 [f] Mwa ici adzazindikira onse kuti
muli akuphunzira anga, ngati muli
naco cikondano wina ndi mnzace.

*Yesu aneneratu kuti Petro adza-mkana.*

(Mat. 26. 33-35. Marko 14. 29-31.
Luka 22. 33, 34.)

36 Simoni Petro anena ndi Iye,
Ambuye, mumuka kuti? Yesu ana-
yankha, Kumene ndimukako sunga-
the kunditsata Ine tsopano; koma,
[j] udzanditsata bwino lomwe. 37 Petro
ananena ndi Iye, Ambuye sindingathe
kukutsatani Inu tsopano cifukwa
ninji? [l] Ndidzataya moyo wanga ci-
fukwa ca Inu. 38 Yesu anayankha,
Moyo wako kodi udzautaya cifukwa
ca Ine? Indetu, indetu, ndinena
kwa iwe, Asanalire tambala udzandi-
kana Ine katatu.

## 14 *Yesu aneneratu za kubwe-ranso kwace.*

(1 Ates. 4. 14-17.)

Mtima wanu usabvutike; mu-
khulupirira Mulungu, khulupirirani
Inenso. 2 M'nyumba ya Atate wa-
nga alimo malo okhalamo ambiri.
Ngati sikudali kutero, ndikadakuuzani
inu; pakuti [s] ndipita kukukonzerani
inu malo. 3 Ndipo ngati ndipita ku-
kakonzera inu malo, [u] ndidzabweranso,
ndipo ndidzalandira inu kwa Ine nde-
kha; kuti [w] kumene kuli Ineko, mu-
kakhale inunso. 4 Ndipo kumene
ndinkako Ine, mudziwa njira yace.
5 Tomasi ananena ndi Iye, Ambuye,
sitidziwa kumene munkako; tidziwa
njira bwanji? 6 Yesu ananena naye,
[y] Ine ndine njira, ndi [z] coonadi, ndi
[a] moyo. [b] Palibe munthu adza kwa
Atate, koma mwa Ine.

*Yesu ndi Atate ndiwo amodzi.*

7 [d] Mukadazindikira Ine mukada-
dziwa Atate wanganso; kuyambira
tsopano mumzindikira Iye, ndipo
mwamuona Iye. 8 Filipo ananena
ndi Iye, Ambuye, tionetsereni ife
Atate, ndipo citikwanira. 9 Yesu
ananena naye, Kodi ndiri ndi inu
nthawi yaikuru yotere, ndipo sunandi-
zindikira, Filipo? [b] Iye amene wa-
ndiona Ine waona Atate; unena iwe
bwanji, Mutionetsere Atate? 10 Su-
khulupirira kodi kuti [e] ndiri Ine mwa
Atate, ndi Atate ali mwa Ine? Mau
amene ndinena Ine kwa inu [e] sindila-
nkhula kwa Ine ndekha; koma Atate
wokhala mwa Ine acita nchito zace.
11 Khulupirirani Ine, [g] kuti Ine ndiri
mwa Atate ndi Atate ali mwa Ine;
koma ngati si comweco, khulupirirani
Ine cifukwa ca nchito zomwe. 12 Inde-
tu, indetu, ndinena kwa inu, [h] Wokhu-
lupirira Ine, nchito zimene ndicita Ine
adzazicitanso iyeyu; ndipo adzacita
zoposa izi; cifukwa ndipita Ine kwa
Atate. 13 Ndipo [i] cimene ciri conse
mukafunse m'dzina langa, ndidzaci-
cita, kuti Atate akalemekezedwe mwa
Mwana. 14 Ngati mudzapempha
kanthu m'dzina langa, ndidzacita.
15 [k] Ngati mukonda Ine, sungani ma-
lamulo anga.

*Lonjezo la Mzimu Woyera.*

16 Ndipo Ine ndidzapempha Atate,
ndipo [m] adzakupatsani inu Nkhoswe
yina, kuti akhale ndi inu ku nthawi
yonse, 17 ndiye [n] Mzimu wa coonadi;
amene dziko lapansi silingathe kumla-
ndira, pakuti silimuona Iye, kapena
kumzindikira Iye. Inu mumzindi-
kira Iye; cifukwa akhala ndi inu
[o] nadzakhala mwa inu. 18 [p] Sindidza-
kusiyani inu mukhale ana amasiye;
ndidza kwa inu. 19 Katsala kanthawi,
ndipo dziko lapansi silindionanso Ine;
koma inu mundiona; [r] popeza Ine
ndiri ndi moyo inunso mudzakhala ndi
moyo. 20 Tsiku lomwelo mudza-
zindikira kuti [t] ndiri Ine mwa Atate
wanga, ndi inu mwa Ine, ndi Ine mwa
inu. 21 [v] Iye wakukhala nao mala-
mulo anga, ndi kuwasunga, iyeyu
ndiye wondikonda Ine; koma wondi-
konda Ine adzakondedwa ndi Atate
wanga, ndipo Ine ndidzamkonda,
ndipo ndidzadzionetsa ndekha kwa
iye. 22 Yudase, si Isikariote, ananena
ndi Iye, Ambuye, cacitika ciani kuti
muziti mudzionetsa nokha kwa ife,
koma si kwa dziko lapansi? 23 Yesu
anayankha nati kwa iye, [c] Ngati wina
akonda Ine, adzasunga mau anga;
ndipo Atate wanga adzamkonda,
ndipo [e] tidzadza kwa iye, ndipo tidza-
yesa kwa iye mokhalamo. 24 Wosa-
ndikonda Ine sasunga mau anga;
ndipo [f] mau amene mumva sali mau
anga, koma a Atate wondituma Ine.
25 Izi ndalankhula nanu, pakukha-
la ndi inu. 26 Koma [g] Nkhosweyo,
Mzimu Woyera, amene Atate adzamtu-

[a] Yoh. 7. 34
[b] Akol. 1. 15
[c] Yoh. 10. 37, 38
[d] Lev. 19. 18 Yoh. 15. 12, 17 1 Yoh. 2. 7, 8
[e] Yoh. 7. 16
[f] 1 Yoh. 4. 20
[g] Yoh. 10. 37, 38
[h] Mat. 21. 21, 22
[i] Mat. 21. 21, 22
[j] Yoh. 21. 18, 22
[k] v. 21, 23
[l] Mat. 26. 33-35
[m] Yoh. 15.26 „ 16.13
[n] Yoh. 15.26 „ 16.13
[o] 1 Yoh. 2. 27
[p] Mat. 28.20
[r] 1 Akor. 15. 20
[s] Yoh. 13. 33, 36
[t] v. 10
[u] Mac. 1. 11
[v] v. 15, 23
[w] Yoh. 17. 24
[y] Ahebr. 10. 20
[z] Yoh. 1. 17
[a] Yoh. 1. 4
[b] Yoh. 10. 9
[c] v. 15
[d] Yoh. 8. 19
[e] Cibv. 3. 20
[f] Yoh. 7. 16
[g] Luka 24. 49 v. 16





ma m'dzina langa, [a] Iyeyo adzaphunzi-
tsa inu zonse, nadzakumbutsa inu zi-
nthu zonse zimene ndinanena kwa inu.

*Mphatso ya mtendere.*

27 [e] Mtendere ndikusiyirani inu,
mtendere wanga ndikupatsani; Ine
sindikupatsani inu monga dziko la-
pansi lipatsa. [f] Mtima wanu usa-
bvutike, kapena usacite mantha.
28 Mwamva kuti Ine ndinanena kwa
inu, [g] Ndimuka, ndipo ndidza kwa
inu. Mukadandikonda Ine, muka-
dakondwera kuti ndipita kwa Atate;
[h] pakuti Atate ali wamkuru ndi Ine.
29 Ndipo tsopano [i] ndakuuzani cisa-
nacitike, kuti pamene citacitika mu-
kakhulupire. 30 Sindidzalankhulanso
zambiri ndi inu, pakuti [l] mkuru wa
dziko lapansi adza; ndipo alibe
kanthu mwa Ine; 31 koma kuti dziko
lapansi lizindikire kuti ndikonda
Atate, ndi kuti [n] ndicita monga mo-
mwe Atate wandilamulira. Nyamu-
kani tizimuka kucokera kuno.

## 15 *Mpesa ndi nthambi zace.*

Ine ndine mpesa weniweni, ndipo
Atate wanga ndiye wam'munda.
2 [p] Nthambi iri yonse ya mwa Ine
yosabala cipatso, aicotsa; ndi iri
yonse yakubala cipatso, aisadza, kuti
ikabale cipatso cocuruka. 3 [t] Mwa-
khala okonzeka tsopano inu cifukwa
ca mau amene ndalankhula ndi inu.
4 [u] Khalani mwa Ine, ndi Ine mwa
inu. Monga nthambi siingathe ku-
bala cipatso pa yokha, ngati siikhala
mwampesa; motere mulibe inunso
ngati simukhala mwa Ine. 5 Ine
ndine mpesa, inu ndinu nthambi zace:
wakukhala mwa Ine, ndi Ine mwa
iye, [w] ameneyo abala cipatso cambiri;
pakuti kopanda Ine simungathe
kucita kanthu. 6 Ngati wina sakhala
mwa Ine, [a] watayika kunja monga
nthambi, nafota; ndipo azisonkha-
nitsa nazitaya kumoto, nazitentha.
7 Ngati mukhala mwa Ine, ndi mau
anga akhala mwa inu, [c] pemphani
cimene ciri conse mucifuna, ndipo
cidzacitika kwa inu. 8 [e] Mwa ici
alemekezedwa Atate wanga, kuti
mubale cipatso cambiri; ndipo mu-
dzakhala akuphunzira anga. 9 Monga
momwe Atate wandikonda Ine, Inenso
ndakonda inu; khalani m'cikondi
canga. 10 [g] Ngati musunga malamulo
anga mudzakhala m'cikondi canga;
monga Ine ndasunga malamulo a
Atate wanga, ndipo ndikhala m'ciko-
ndi cace. 11 Izi ndalankhula ndi
inu, [b] kuti cimwemwe canga cikhale
mwa inu, ndi kuti cimwemwe canu
cidzale. 12 [c] Lamulo langa ndi ili,
kuti mukondane wina ndi mnzace,
monga ndakonda inu. 13 [d] Palibe
munthu ali naco cikondi coposa ici
cakuti munthu ataya moyo wace ci-
fukwa ca abwenzi ace. 14 Muli
abwenzi anga inu, ngati muzicita
zimene ndikulamulirani inu.

*Ciyanjano catsopano.*

15 Sindichanso inu akapolo; cifu-
kwa kapolo sadziwa cimene mbuye
wace acita; koma ndacha inu abwe-
nzi; [j] cifukwa zonse zimene ndazi-
mva kwa Atate wanga ndakudziwi-
tsani. 16 [k] Inu simunandisankha Ine,
koma Ine ndinakusankhani inu, ndipo
ndinakuikani, kuti mukamuke inu ndi
kubala cipatso, ndi kuti cipatso canu
cikhale; kuti [m] cimene ciri conse
mukapempha Atate m'dzina langa
akakupatseni inu. 17 [o] Zinthu izi
ndilamulira inu, kuti mukondane
wina ndi mnzace.

*Wokhulupirira pokhala pa dziko lapansi.*

18 [r] Ngati dziko lapansi lida inu,
mudziwa kuti lidada Ine lisanayambe
kuda inu. 19 [s] Mukadakhala a dziko
lapansi, dziko lapansi likadakonda
zace za lokha; koma popeza simuli a
dziko lapansi, koma Ine ndinakusa-
nkhani inu mwa dziko lapansi, cifukwa
ca ici likudani inu. 20 [v] Kumbukilani
mau amene Ine ndinanena kwa inu,
Kapolo sali wamkuru ndi mbuye wace.
Ngati anandilondalonda Ine, adzaku-
londa-londani inunso; ngati anasunga
mau anga, adzasunga anunso. 21 Ko-
ma [y] izi zonse adzakucitirani cifukwa
ca dzina langa, cifukwa sadziwa
wondituma Ine. 22 [z] Sindikadadza
ndi kulankhula nao sakadakhala nalo
cimo; koma tsopano alibe cowiri-
ngula pa macimo ao. 23 [b] Iye
wondida Ine, adanso Atate wanga.
24 [d] Sindikadacita mwa iwo nchito
zosacita wina, sakadakhala nalo cimo;
koma tsopano anaona nada Ine ndi
Atate wanganso. 25 Koma citero,
kuti mau olembedwa m'cilamulo cao
akwaniridwe, kuti, [f] Anandida Ine
kopanda cifukwa.

*Mzimu Woyera ndi akuphu-nzira omwe adzacita umboni.*

26 Koma [h] pamene wafika Nkhoswe,
amene Ine ndidzamtuma kwa inu

[a] Yoh. 16.13
[b] Yoh. 16.24
[c] 1 Yoh. 3. 11
[d] Yoh. 10. 11, 15 Aroma 5. 7, 8
[e] Afil. 4. 7
[f] v. 1
[g] v. 3, 18
[h] Yoh. 10. 29, 30
[i] Yoh. 16. 4
[j] Mac. 20.27
[k] 1 Yoh. 4. 10, 19
[l] Yoh. 12. 31
[m] v. 7
[n] Afil. 2. 8
[o] 1 Yoh. 3. 11
[p] Mat. 15.13
[r] 1 Yoh. 3, 1, 13
[s] Yoh. 17. 14 1 Yoh. 4.5
[t] Yoh. 17. 17
[u] Akol. 1.23
[v] Mat. 10.24
[w] Afil. 1. 11
[y] Mat. 10.22
[z] Yoh. 9. 41
[a] Mat. 7. 19
[b] 1 Yoh. 2. 23
[c] Yoh. 14. 13, 14
[d] Yoh. 9. 32
[e] Mat. 5. 16
[f] Sal. 69. 4
[g] Yoh. 14. 15, 21, 23
[h] Yoh. 14. 17, 26 „ 16. 7, 13

kucokera kwa Atate, ndiye Mzimu wa
coonadi, amene aturuka kwa Atate,
Iyeyu adzandicitira Ine umboni.
27 Ndipo [a] inunso mucita umboni, pa-
kuti muli ndi Ine kuyambira ciyambi.

## 16 *Awacenjeza za kuzunzidwa.*
(Mat. 24. 9, 10. Luka 21. 16-19.)

Izi ndalankhula ndi inu kuti [b] mu-
ngakhumudwitsidwe. 2 [c] Adzakutu-
rutsani m'masunagoge; koma ikudza
nthawi imene [d] yense wakupha inu
adzayesa kuti atumikira Mulungu.
3 Ndipo izi adzacita, [e] cifukwa sana-
dziwa Atate, kapena Ine. 4 Koma
[f] zinthu izi ndalankhula ndi inu kuti
ikadza nthawi yao, mukakumbukire
kuti ndinakuuzani. Koma izi sindi-
nanena kwa inu kuyambira paci-
yambi, cifukwa ndinali pamodzi ndi
inu. 5 Koma [g] tsopano ndimuka
kwa Iye wondituma Ine; ndipo
palibe wina mwa inu andifunsa Ine,
Munka kuti? 6 Koma cifukwa nda-
lankhula izi ndi inu [h] cisoni cadzala
mumtima mwanu.

*Comwe Mzimu Woyera adza-
citira anthu.*

7 Koma ndinena Ine coonadi ndi
inu; kuyenera kwa inu kuti ndicoke
Ine; pakuti ngati sindicoka, Nko-
sweyo sadzadza kwa inu; koma
[k] ngati ndipita ndidzamtuma Iye kwa
inu. 8 Ndipo atadza Iyeyo, adza-
tsutsa dziko lapansi za macimo, ndi
za cilungamo, ndi za ciweruziro;
9 za macimo, cifukwa sakhulupirira
Ine; 10 za cilungamo, cifukwa ndi-
nka kwa Atate, ndipo simundiona-
nso; 11 za ciweruziro, cifukwa mkuru
wa dziko ili lapansi waweruzidwa.
12 Ndiri nazo zambirinso zakunena
kwa inu, koma simungathe kuzisenza
tsopano lino. 13 Koma atadza Iyeyo,
Mzimu wa coonadi, [o] adzatsogolera inu
m'coonadi conse; pakuti sadzala-
nkhula za Iye mwini; koma zinthu
ziri zonse adzazimva, adzazilankhula;
ndipo zinthu zirinkudza adzakulali-
kirani. 14 Iyeyo adzalemekeza Ine;
cifukwa adzatenga za mwa Ine,
nadzalalikira kwa inu. 15 [s] Zinthu
ziri zonse Atate ali nazo ndi zanga;
cifukwa cace ndinati, kuti atenga za
mwa Ine, nadzalalikira kwa inu.

*Yesu anena za imfa, kuuka, ndi
kubwera kwace.*

16 [v] Katsala kanthawi, ndipo simu-
ndionanso Ine, ndipo kanthawinso,
ndipo mudzandiona Ine. 17 Mwa
akuphunzira ace tsono anati wina ndi
mnzace, Ici nciani cimene anena ndi
ife, Kanthawi ndipo simundiona; ndi-
ponso kanthawi, ndipo mudzandiona;
ndipo, cifukwa ndimuka kwa Atate?
18 Cifukwa cace ananena, Ici nciani
cimene anena, Kanthawi? Sitidziwa
cimene alankhula. 19 Yesu anazi-
ndikira kuti analikufuna kumfunsa
Iye, ndipo anati kwa iwo, Kodi muli-
kufunsana wina ndi mnzace za ici,
kuti ndinati, Kanthawi ndipo simu-
ndiona Ine, ndiponso kanthawi nimu-
dzandiona Ine? 20 Indetu, indetu,
ndinena ndi inu, kuti mudzalira
ndi kubuma maliro inu, koma dziko
lapansi lidzakondwera; mudzacita
cisoni inu, koma cisoni canu cidza-
sandulika cimwemwe. 21 Mkazi
pamene akuti abale ali naco cisoni,
cifukwa yafika nthawi yace; koma
pamene wabala mwana, sakumbuki-
lanso kusaukako, cifukwa ca cimwe-
mwe kuti wabadwa munthu ku dziko
lapansi. 22 Ndipo inu tsono muli
naco cisoni tsopano lino, koma ndidza-
kuonaninso, ndipo [i] mtima wanu
udzakondwera, ndipo palibe wina
adzacotsa kwa inu cimwemwe canu.
23 Ndipo tsiku limenelo simudzandi-
funsa kanthu. Indetu, indetu, ndi-
nena kwa inu, [j] Ngati mudzapempha
Atate kanthu, adzakupatsani inu
m'dzina langa. 24 Kufikira tsopano
simunapempha kanthu m'dzina langa;
pemphani, ndipo mudzalandira, [l] kuti
cimwemwe canu cikwaniridwe.
25 Zinthu izi ndalankhula ndi inu
m'mafanizo; ikudza nthawi imene
sindidzalankhula ndi inu m'mafanizo,
koma ndidzakulalikirani inu momve-
ka za Atate. 26 [m] Tsiku limenelo
mudzapempha m'dzina langa; ndipo
sindinena kwa inu kuti Ine ndidza-
funsira inu kwa Atate; 27 pakuti
[n] Atate yekha akonda inu, cifukwa
inu mwandikonda Ine, ndi [p] kukhulu-
pirira kuti Ine ndinaturuka kwa
Atate. 28 [r] Ndinaturuka mwa Atate,
ndipo ndadza ku dziko lapansi: ndi-
lisiyanso dziko lapansi, ndipo ndipita
kwa Atate. 29 Akuphunzira ace ana-
nena, Onani, tsopano mulankhula
zomveka, ndipo mulibe kunena ci-
phiphiritso. 30 Tsopano tidziwa kuti
[t] mudziwa zonse, ndipo mulibe kuso-
wa kuti wina akafunse Inu; mwa
ici tikhulupirira kuti munaturuka
kwa Mulungu. 31 Yesu anayankha
iwo, Kodi mukhulupirira tsopano?
32 [u] Onani ikudza nthawi, ndipo ya-
fika, imene mudzabalalitsidwa, yense
ku zace za yekha, ndipo mudzandisiya

[a] Mac. 1. 8 Luka 1. 2
[b] Mat. 11. 6
[c] Yoh. 12. 42
[d] Mac. 8. 1 ,, 9. 1.
[e] Yoh. 15. 21
[f] Yoh. 14. 29
[g] Yoh. 14. 28
[h] Yoh. 14. 1
[i] Luka 24. 41, 52
[j] Yoh. 15. 16
[k] Mac. 2. 33
[l] Yoh. 15. 11
[m] v. 23
[n] Yoh. 14. 21, 23
[o] Yoh. 14. 26 1 Yoh. 2. 20, 27
[p] Yoh. 17. 8
[r] Yoh. 13. 3
[s] Mat. 11. 27
[t] Yoh. 21. 17
[u] Mat. 26. 13 Marko 14. 50
[v] Yoh. 13. 3, 33





Ine pa ndekha. Ndipo [a] sindikhala
pa ndekha, cifukwa Atate ali pamodzi
ndi Ine, 33 Zinthu izi ndalankhula ndi
inu, kuti [b] mwa Ine mukakhale nao
mtendere. [d] M'dziko lapansi mudza-
khala naco cibvuto, koma limbikani
mtima; [e] ndalilaka dziko lapansi Ine.

## 17 *Yesu apempherera akuphu-nzira ace.*

Zinthu izi analankhula Yesu;
ndipo m'mene anakweza maso ace
Kumwamba, anati, Atate, [i] yafika
nthawi; lemekezani Mwana wanu,
kuti Mwana wanu akulemekezeni
Inu; 2 [j] monga mwampatsa Iye ula-
muliro pa thupi liri lonse, kuti onse
amene mwampatsa Iye, awapatse iwo
moyo wosatha. 3 Koma [l] moyo wo-
satha ndi uwu, kuti akadziwe Inu
Mulungu woona yekha, ndi Yesu
Kristu [m] amene munamtuma. 4 Ine
ndalemekeza Inu pa dziko lapansi,
[n] m'mene ndinatsiriza nchito imene
munandipatsa ndicite. 5 Ndipo tso-
pano, Atate Inu, lemekezani Ine ndi
Inu nokha [p] ndi ulemerero umene
ndinali nao ndi Inu lisanakhale
dziko lapansi. 6 Ndalionetsera dzina
lanu kwa anthu [s] amene mwandipa-
tsa Ine m'dziko lapansi; anali anu,
ndipo mwandipatsa Ine iwo; ndipo
adasunga mau anu. 7 Azindikira
tsopano kuti zinthu ziri zonse zimene
mwandipatsa Ine zicokera kwa Inu;
8 cifukwa [u] mau amene munandipa-
tsa Ine ndinapatsa iwo; ndipo anala-
ndira, [z] nazindikira koona kuti ndina-
turuka kwa Inu, ndipo anakhulupira
kuti Inu munanditumа Ine. 9 Ine
ndiwapempherera iwo; sindipemphe-
rera dziko lapansi, koma iwo amene
mwandipatsa Ine, 10 cifukwa ali anu:
ndipo [a] zanga zonse ziri zanu, ndi za-
nu ziri zanga; ndipo ndilemekezedwa
mwa iwo. 11 Sindikhalanso m'dziko
lapansi, koma iwo ali m'dziko la-
pansi, ndipo Ine ndidza kwa Inu.
[e] Atate Woyera, sungani awa m'dzina
lanu amene mwandipatsa Ine, kuti
akhale mmodzi, monga Ife. 12 Pa-
mene ndinakhala nao Ine [f] ndina-
likuwasunga iwo m'dzina lanu amene
mwandipatsa Ine; ndipo ndinawa-
sunga, ndipo [g] sanatayika mmodzi
yense wa iwo, koma [h] mwana wa
citayiko, kuti [i] lembo likwaniridwe.
13 Koma tsopano ndidza kwa Inu;
ndipo izi ndilankhula m'dziko lapansi,
kuti akhale naco cimwemwe canga co-
kwaniridwa mwa iwo okha. 14 [k] Ine
ndawapatsa iwo mau anu; ndipo
[n] dziko lapansi linadana nao, cifu-
kwa sakhala a dziko lapansi, monga
Ine sindikhala wa dziko lapansi.
15 Sindipempha kuti muwacotse iwo
m'dziko lapansi, koma kuti [e] muwa-
sunge iwo kuletsa woipayo. 16 Siali
a dziko lapansi monga Ine sindiri
wa dziko lapansi. 17 [f] Patulani iwo
m'coonadi; mau anu ndi coonadi.
18 [g] Monga momwe munanditumа Ine
ku dziko lapansi, Inenso ndinatuma
iwo ku dziko lapansi. 19 Ndipo
[h] cifukwa ca iwo Ine ndidzipatula
ndekha kuti iwonso akhale opatulidwa
m'coonadi. 20 Koma sindipemphe-
rera iwo okha, komanso iwo aku-
khulupirira Ine cifukwa ca mau ao;
21 [k] kuti onse akakhale amodzi, mo-
nga Inu Atate mwa Ine, ndi Ine mwa
Inu, kuti iwonso akakhale mwa Ife:
kuti dziko lapansi likakhulupire kuti
Inu munanditumа Ine. 22 Ndipo
ulemerero umene mwandipatsa Ine
ndapatsa iwo; [k] kuti akhale amodzi,
monga Ife tiri mmodzi; 23 Ine
mwa iwo, ndi Inu mwa Ine, [o] kuti
akhale angwiro mwa mmodzi; kuti
dziko lapansi lizindikire kuti Inu
munanditumа Ine, nimunawakonda
iwo, monga momwe munakonda
Ine. 24 [r] Atate, amene mwandipatsa
Ine, ndifuna kuti, kumene ndiri Ine,
iwonso akhale pamodzi ndi Ine;
kuti ayang'anire ulemerero wanga,
umene mwandipatsa Ine; [t] pakuti
munandikonda Ine lisanakhazikike
dziko lapansi. 25 Atate wolungama,
[v] dziko lapansi silinadziwa Inu, koma
[w] Ine ndinadziwa Inu; ndipo [y] iwo
anazindikira kuti munanditumа Ine;
26 ndipo [a] ndinazindikiritsa iwo dzina
lanu, ndipo ndidzalizindikiritsa; kuti
cikondi [b] cimene munandikonda naco
cikhale mwa iwo, ndi Ine mwa iwo.

## 18 *Yesu m'Getsemane.*
(Mat. 26. 36-46. Marko 14. 32-42. Luka 22. 39-46.)

M'mene Yesu adanena izi, [d] ana-
turuka ndi akuphunzira ace, kunka
tsidya lija la mtsinje wa Kedroni,
kumene kunali munda, umene ana-
lowamo Iye ndi akuphunzira ace.

*Aperekedwa namangidwa.*
(Mat. 26. 47-56. Marko 14. 43-50. Luka 22. 47-53.)

2 Koma Yudasenso amene akampe-
reka Iye, anadziwa malowa; [j] cifu-
kwa Yesu akamkako kawiri kawiri
ndi akuphunzira ace. 3 [l] Pamenepo
Yudase, m'mene adatenga gulu la
asilikari, ndi anyamata kwa ansembe

[a] Yoh. 8. 29
[b] Yes. 9. 6 Akol. 1. 20
[c] Mat. 6. 13 Agal. 1. 4
[d] Yoh. 15. 18-21
[e] Aroma 8. 37 1 Yoh. 4. 4
[f] Aefeso 5. 26
[g] Yoh. 20. 21
[h] 1 Akor. 1. 2, 30
[i] Yoh. 12. 23
[j] Mat. 11. 27
[k] Yoh. 10. 16, 38 Aroma 12. 5 1 Yoh 1. 3
[l] 1 Yoh. 5. 20
[m] Yoh. 3. 34
[n] Yoh. 5. 36 ,, 9. 3
[o] Akol. 3. 14
[p] Yoh. 1. 1, 2
[r] Yoh. 12. 26 ,, 14. 3 1 Ates. 4. 17
[s] v. 2, 9, 11
[t] v. 5
[u] Yoh. 8. 28
[v] Yoh. 15. 21
[w] Yoh. 7. 29
[y] Yoh. 16. 27
[z] Yoh. 16. 27, 30
[a] Yoh. 15. 15
[b] Yoh. 15. 9
[c] Yoh. 16. 15
[d] 2 Sam. 15. 23 Mat. 26. 36
[e] 1 Petr. 1. 5 Yuda 1
[f] Yoh. 6. 39
[g] Yoh. 18. 9
[h] Yoh. 6. 70
[i] Mac. 1. 20
[j] Luka 21. 37
[k] v. 8
[l] Mat. 26. 47
[m] Yoh. 15. 18, 19

akulu ndi Afarisi, anadza komweko
ndi nyali ndi miuni ndi zida. 4 Pa-
menepo Yesu, podziwa zonse ziri-
nkudza pa Iye, anaturuka, nati kwa
iwo, Mufuna yani? 5 Anayankha
Iye, Yesu Mnazarayo. Yesu ananena
nao, Ndine. Koma Yudase yemwe,
wompereka Iye, anaima nao pa-
modzi. 6 Ndipo m'mene anati kwa
iwo, Ndine, anabwerera m'mbuyo,
nagwa pansi. 7 Pamenepo anawa-
funsanso, Mufuna yani? koma iwo
anati, Yesu Mnazarayo. 8 Yesu
anayankha, Ndati, Ndine; cifukwa
cace ngati mufuna Ine, lekani awa
amuke; 9 kuti akwaniridwe mau
amene ati, [c] Mwa iwo amene mwandi-
patsa Ine, sindinataya mmodzi.
10 [d] Pamenepo Simoni Petro pokhala
nalo lupanga, analisolola nakantha
kapolo wa mkulu wa ansembe, namse-
nga khutu lace lamanja. Koma
dzina lace la kapoloyo ndiye Malko.
11 Pamenepo Yesu anati kwa Petro,
Longa lupanga m'cimake cace; [f] cikho
cimene Atate wandipatsa Ine sindi-
mwere ici kodi?

*Yesu kwa mkulu wa ansembe.*
*Petro amkana.*

(Mat. 26. 57-75. Marko 14. 53-72.
Luka 22. 54-71.)

12 Ndipo khamulo ndi kapitao
wamkuru, ndi anyamata a Ayuda
anagwira Yesu nammanga Iye,
13 [h] nayamba kupita naye kwa Anasi;
pakuti anali mpongozi wa Kayafa,
amene anali mkulu wa ansembe caka
comweco. 14 Koma [j] Kayafa, anali
uja wakulangiza Ayuda, kuti kuye-
nera munthu mmodzi afere anthu.
15 Koma [l] Simoni Petro ndi wo-
phunzira wina anatsata Yesu. Koma
wophunzira ameneyo anali wodziwi-
ka kwa mkulu wa ansembe, nalowa
pamodzi ndi Yesu m'bwalo la mkulu
wa ansembe; 16 koma [m] Petro anai-
ma kukhomo kunja. Cifukwa cace
wophunzira winayo amene anadzi-
wika kwa mkulu wa ansembe, anatu-
ruka nalankhula ndi wapakhomo, na-
lowetsa Petro. 17 Pamenepo namwali
wapakhomoyo ananena kwa Petro,
Kodi suli iwenso wa akuphunzira
a munthu uyu? Iyeyu ananena,
Sindine. 18 Koma akapolo ndi anya-
mata analikuimirirako, atasonkha
moto wamakara; pakuti kunali ku-
zizira; ndipo analikuotha moto;
koma Petronso anali nao alikuimi-
rira ndi kuotha moto.
19 Ndipo mkulu wa ansembe ana-
funsa Yesu za akuphunzira ace, ndi
ciphunzitso cace. 20 Yesu anayankha
iye, [a] Ine ndalankhula zomveka kwa
dziko lapansi; ndinaphunzitsa Ine
nthawi zonse m'sunagoge ndi m'ka-
cisi, kumene amasonkhana Ayuda
onse; ndipo mobisika sindinalankhu-
la kanthu. 21 Undifunsiranji Ine?
funsa iwo amene adamva cimene
ndinalankhula nao; taona, amene-
wo adziwa cimene ndinanena Ine.
22 Koma m'mene Iye adanena izi,
[b] mmodzi wa anyamata akuimirirako
anapanda Yesu khofu, ndi kuti, Kodi
uyankha mkulu wa ansembe co-
mweco? 23 Yesu anayankha iye,
Ngati ndalankhula coipa, cita umboni
wa coipaco, koma ngati bwino, undi-
pandiranji? 24 Koma Anasi ada-
mtumiza Iye womangidwa kwa Kayafa
mkulu wa ansembe.
25 Koma Simoni Petro analikui-
mirira ndi kuotha moto. Pomwepo
anati kwa iye, [e] Suli iwenso wa aku-
phunzira ace kodi? Iyeyu anakana,
nati, Sindine. 26 Mmodzi wa akapolo
a mkulu wa ansembe ndiye mbale
wace wa uja amene Petro anamdula
khutu, ananena, Ine sindinakuona
iwe kodi m'munda pamodzi ndi Iye?
27 Pamenepo Petro anakananso;
ndipo [g] pomwepo analira tambala.

*Yesu kwa Pilato.*

(Mat. 27. 1, 2, 11-31. Marko 15. 1-20.
Luka 23. 1-7, 13-25.)

28 [i] Pamenepo anamtenga Yesu
kucokera kwa Kayafa kupita ku
Pretorio; koma munali mamawa;
ndipo [k] iwo sanalowa ku Pretorio, kuti
angadetsedwe, koma kuti akadye
Paskha. 29 Cifukwa cace Pilato ana-
turukira kunja kwa iwo, nati, Cifu-
kwa canji mwadza naco ca munthu
uyu? 30 Anayankha nati kwa iye,
Akadakhala wosacita zoipa uyu siti-
kadampereka Iye kwa inu. 31 Ndipo
Pilato anati kwa iwo, Mumtenge Iye
inu, ndi kumweruza Iye monga mwa
cilamulo canu. Ayuda anati kwa iye,
Tiribe ulamuliro wakupha munthu ali
yense; 32 kuti mau a Yesu akwaniri-
dwe, [n] amene ananena akuzindikiritsa
imfa imene akuti adzafa nayo.
33 [o] Cifukwa cace Pilato analowa-
nso m'Pretorio, naitana Yesu, nati
kwa Iye, Iwe ndiwe Mfumu ya Ayuda
kodi? 34 Yesu anayankha, Kodi
munena ici mwa inu nokha, kapena
ena anakuuzani za Ine? 35 Pilato
anayankha, Ndiri ine Myuda kodi?
Mtundu wako ndi ansembe akulu ana-
kupereka kwa ine; wacita ciani?
36 Yesu anayankha, [p] Ufumu wanga

[a] Mat. 26. 55
[b] Yer. 20. 2 Mac. 23. 2
[c] Yoh. 17. 12
[d] Mat. 26. 51
[e] Mat. 26. 69, 71
[f] Mat. 20. 22 „ 26. 39, 42
[g] Mat. 26. 74
[h] Luka 3. 2
[i] Mat. 27. 2
[j] Yoh. 11. 50
[k] Mac. 10. 28
[l] Mat. 26. 58
[m] Mat. 26. 69
[n] Mat. 20. 18, 19
[o] Mat. 27. 11
[p] Luka 12. 14





suli wa dziko lino lapansi; ufumu
wanga ukadakhala wa dziko lino
lapansi, anyamata anga akadalimbika
nkhondo, kuti ndisaperekedwe kwa
Ayuda; koma tsopano ufumu wanga
suli wocokera konkuno. 37 Pame-
nepo Pilato anati kwa Iye, Nanga
kodi ndiwe Mfumu? Yesu anaya-
nkha, Munena kuti ndine Mfumu.
Ndinabadwira ici Ine, ndipo ndina-
dzera ici kudza ku dziko lapansi, kuti
ndikacite umboni ndi coonadi. [b] Yense
wakukhala mwa coonadi amva mau
anga. 38 Pilato ananena kwa Iye,
Coonadi nciani?
Ndipo pamene adanena ici, ana-
turukiranso kwa Ayudawo, nanena
nao, [c] Ine sindipeza konse cifukwa
mwa Iye. 39 Koma [d] muli nao ma-
khalidwe, akuti ndimamasulira inu
mmodzi pa Paskha; kodi mufuna
tsono kuti ndimasulire inu Mfumu ya
Ayuda? 40 [f] Pomwepo anapfuula-
nso, nanena, Si uyu, koma Baraba.
Koma [h] Baraba anali wacifwamba.

19 Pamenepo tsono [i] Pilato ana-
tenga Yesu, namkwapula.
2 Ndipo asilikari, m'mene [j] analuka
korona waminga anambveka pa-
mutu pace, nampfunda Iye maraya
acibakuwa; 3 nadza kwa iye, na-
nena, [l] Tikuoneni, Mfumu ya Ayuda!
nampanda khofu. 4 Ndipo Pilato
anaturukanso kunja, nanena nao,
Taonani, ndidza naye kwa inu ku-
nja [n] kuti mudziwe kuti sindipeza
mwa Iye cifukwa ciri conse. 5 Pa-
menepo Yesu anaturuka kunja, ata-
bvala korona waminga, ndi maraya
acibakuwa. Ndipo ananena nao,
Taonani munthuyu! 6 Ndipo [p] pa-
mene ansembe akulu ndi anyamata
anamuona Iye, anapfuula nanena,
Mpacikeni, mpacikeni. Pilato ana-
nena nao, Mtengeni Iye inu ni-
mumpacike; pakuti ine sindipeza
cifukwa mwa Iye. 7 Ayuda ana-
myankha iye, [r] Tiri naco cilamulo
ife, ndipo monga mwa cilamuloco
ayenera kufa, [s] cifukwa anadziyesera
Mwana wa Mulungu. 8 Ndipo pa-
mene Pilato anamva mau awa, anao-
pa koposa. 9 Ndipo analowanso ku
Pretorio, nanena kwa Yesu, Mucoka
kuti? koma [u] Yesu sanamyankha
kanthu. 10 Cifukwa cace Pilato
ananena kwa Iye, Simulankhula ndi
ine kodi? simudziwa kodi kuti ula-
muliro ndiri nao wakukumasulani,
ndipo ndiri nao ulamuliro waku-
kupacikani? 11 Yesu anamyankha
iye, [w] Simukadakhala nao ulamuliro
uli wonse pa Ine, ngati sukadapatsi-
dwa kwa inu kucokera Kumwamba;
cifukwa ca ici iye wondipereka Ine
kwa inu ali nalo cimo loposa. 12 Pa
ici Pilato anafuna kumasula Iye;
koma Ayuda anapfuula, ndi kunena,
[a] Ngati mumasula ameneyo, simuli
bwenzi la Kaisara; yense wodzi-
yesera yekha Mfumu atsutsana na-
ye Kaisara. 13 Pamenepo Pilato,
m'mene adamva mau awa, anaturuka
ndi Yesu, nakhala pansi pa mpando
woweruzira kumalo dzina lace,
Bwalo lamiyala, koma m'Cihebri,
Gabata. 14 Koma linali tsiku lokonza
Paskha; panali monga ora lacisanu
ndi cimodzi. Ndipo ananena kwa
Ayuda, Taonani, Mfumu yanu!
15 Pamenepo anapfuula iwowa,
Cotsani, Cotsani, mpacikeni Iye!
Pilato ananena nao, Ndipacike
Mfumu yanu kodi? Ansembe akulu
anayankha, [e] Tiribe Mfumu koma
Kaisara. 16 Ndipo [g] pamenepo ana-
mpereka Iye kwa iwo kuti ampacike.

*Ampacika Yesu pamtanda*

(Mat. 27. 32-56. Marko 15. 22-39.
Luka 23. 33-47.)

Pamenepo anatenga Yesu; 17 ndipo
anasenza mtanda yekha, [k] naturuka
kunka ku malo ochedwa Malo-a-
bade, amene achedwa m'Cihebri,
Golgota: 18 kumene anampacika
Iye; ndipo [m] pamodzi ndi Iye awiri
ena, cakuno ndi cauko, koma Yesu
pakati. 19 Koma [o] Pilato analemba
lembo, naliika pamtanda. Koma pa-
nalembedwa, YESU MNAZARAYO,
MFUMU YA AYUDA. 20 Ndipo
lembo ilo analiwerenga ambiri a
Ayuda; cifukwa malo amene Yesu
anapacikidwapo anali pafupi pa mu-
dziwo; ndipo linalembedwa m'Cihebri,
ndi m'Ciroma, ndi m'Cihelene. 21 Pa-
menepo ansembe akulu a Ayuda,
ananena kwa Pilato, Musalembe,
Mfumu ya Ayuda; koma kuti Iyeyu
anati, Ndiri Mfumu ya Ayuda.
22 Pilato anayankha, Cimene nda-
lemba ndalemba.
23 [t] Pamenepo asilikari, m'mene
adapacika Yesu, anatenga zobvala
zace, nadula panai, natenga wina
cina, wina cina, ndiponso maraya;
koma maraya anaombedwa monsemo
kuyambira pamwamba pace, analibe
msoko. 24 Cifukwa cace anati
wina kwa mnzace, Tisang'ambe awa,
koma ticite maere, awa akhale a
yani; kuti lembo likwaniridwe limene
linena, [v] Anagawana zobvala zanga
mwa iwo okha, ndi pa maraya anga
anacitira maere. Ndipo asilikari

[a] Luka 23. 2 Mac. 17. 7
[b] 1 Yoh. 4. 6
[c] Mat. 27. 24
[d] Mat. 27. 15
[e] Gen. 49. 10
[f] Mac. 3. 14
[g] Mat. 27. 26, 31
[h] Luka 23. 18, 19
[i] Mat. 20. 19 „ 27. 26.
[j] Mat. 27. 29
[k] Mat. 27. 33
[l] Mat. 27. 29
[m] Mat. 27. 38
[n] Yoh. 18. 38 v. 6
[o] Mat. 27. 37
[p] Mac. 3. 13-15
[r] Lev. 24. 16
[s] Mat. 26. 65
[t] Mat. 27. 35
[u] Yes. 53. 7 Mat. 27. 12, 14
[v] Sal. 22 18
[w] Luka 22. 53

anacita izi. 25 Koma [a] pamtanda
wa Yesu anaimirira amace, ndi
mbale wa amace, Mariya, mkazi
wa Kleopa, ndi Mariya wa Maga-
dala. 26 Pamenepo Yesu [b] pakuona
amace, ndi wophunzira amene ana-
mkonda, alikuimirirako, ananena kwa
amace, [c] Mkazi, taonani, mwana
wanu! 27 Pamene ananena kwa
wophunzirayo, Taona, amai wako.
Ndipo kuyambira ora lomweli wo-
phunzirayo ananka naye kwao.
28 Citapita ici Yesu, podziwa kuti
zonse zidatha pomwepo kuti lembo
likwaniridwe, ananena, [e] Ndimva lu-
dzu. 29 Kunaikidwako cotengera
codzala ndi vinyo wosasa; cifukwa
cace [f] anazenenga cinkhupule co-
dzaza ndi vinyo wosasayo pa phesi
lahisope, nacifikitsa kukamwa kwace.
30 Pamene Yesu tsono adalandira
vinyo wosasayo anati, [h] Kwatha;
ndipo anawerama mutu, napereka
mzimu.

*Satyola miyendo ya Yesu.*

31 Pomwepo Ayuda, [j] popeza pa-
nali tsiku lokonzera, kuti [k] mitembo
ingatsale pamtanda tsiku la Sabata,
pakuti tsiku lomwelo la Sabata linali
lalikuru, anapempha Pilato kuti mi-
yendo yao ityoledwe, ndipo aco-
tsedwe. 32 Cifukwa cace anadza
asilikari natyola miyendo ya woya-
mbayo, ndi ya winayo wopacikidwa
pamodzi ndi Iye; 33 koma pofika
kwa Yesu, m'mene anamuona Iye,
kuti wafa kale, sanatyola miyendo
yace; 34 koma mmodzi wa asilikari
anamgwaza ndi nthungo m'nthiti
yace, ndipo [o] panaturuka pomwepo
mwazi ndi madzi. 35 Ndipo [p] iye
amene anaona, wacita umboni, ndi
umboni wace uli woona; ndipo iye-
yu adziwa kuti anena zoona, kuti
inunso mukakhulupire. 36 Pakuti
izi zinacitika, kuti lembo likwaniri-
dwe, [s] Pfupa la Iye silidzatyoledwa.
37 Ndipo linenanso lembo lina, [t] Adza-
yang'ana pa Iye amene anampyoza.

*Kuikidwa kwa Yesu.*
(Mat. 27. 57-60. Marko 15. 43-47.
Luka 23. 50-56.)

38 [v] Citatha ici Yosefe wa ku Ari-
mateya, ndiye wophunzira wa Yesu,
koma mobisika, cifukwa ca kuopa
Ayuda, anapempha Pilato kuti aka-
cotse mtembo wa Yesu. Ndipo
Pilato analola. Cifukwa cace ana-
dza, nacotsa mtembo wace. 39 Koma
anadzanso [w] Nikodemo, amene anadza
kwa Iye usiku poyamba paja, aliku-
tenga cisanganizo ca mure ndi aloe,
monga miyeso zana. 40 Pamenepo
anatenga mtembo wa Yesu, nauze-
nenga ndi nsaru zabafuta pamodzi
ndi zonunkhira, monga mwa maiki-
dwe a maliro a Ayuda. 41 Koma
kunali munda kumalo kumene ana-
pacikidwako, ndi m'mundamo mu-
nali manda atsopano m'mene sanai-
kidwamo munthu ali yense nthawi
zonse. 42 [d] Pomwepo ndipo anaika
Yesu, cifukwa ca tsiku lokonzera la
Ayuda, pakuti mandawo anali pafupi.

## 20 *Yesu auka kwa akufa.*
(Mat. 28. 1-10. Marko 16. 1-14.
Luka 24. 1-43.)

Koma [g] tsiku loyamba la Sabata
anadza Mariya wa Magadala mama-
wa, kusanayambe kuca, kumanda,
napenya mwala wocotsedwa kuma-
nda. 2 Pomwepo anathamanga nadza
kwa Simoni Petro ndi kwa [i] wophu-
nzira wina amene Yesu anamkonda,
nanena nao, Anacotsa Ambuye ku-
manda, ndipo sitidziwa kumene ana-
muika Iye. 3 [l] Anaturuka tsono
Petro ndi wophunzira winayo, nali-
nkupita kumanda. 4 Koma anatha-
manga onse awiri pamodzi; ndipo
wophunzira winayo anathamanga
naposa Petro, nayamba kufika ku-
manda; 5 ndipo m'mene anawerama
cosuzumira [m] anaona nsaru zabafuta
zitakhala, komatu sanalowamo.
6 Pamenepo anadzanso Simoni Petro
alikumtsata iye, nalowa m'manda;
ndipo anaona nsaru zabafuta zita-
khala, 7 ndi [n] mlezo, umene unali
pamutu pace, wosakhala pamodzi ndi
nsaru zabafuta, koma wopindika
padera pamalo pena. 8 Pamenepo
tsono analowanso wophunzira winayo,
amene anayamba kufika kumanda,
ndipo anaona, nakhulupira. 9 Pakuti
kufikira pomwepo [r] sanadziwa lembo
lakuti ayenera Iye kuuka kwa akufa.
10 Cifukwa cace akuphunzirawo ana-
cokanso, kunka kwao.

*Yesu aonekera kwa Mariya wa Magadala.*

11 Koma [u] Mariya analikuima ku-
manda kunja, alikulira. Ndipo
m'mene alikulira anawerama cisuzu-
mirire kumanda; 12 ndipo anaona
angelo awiri atabvala zoyera, aliku-
khala mmodzi kumutu, ndi wina ku-
miyendo, kumene mtembo wa Yesu
udagona. 13 Ndipo iwowa ananena
kwa iye, Mkazi, uliranji? Ananena

[a] Mat.27.55
[b] Yoh.13.23
„ 20. 2
[c] Yoh. 2. 4
[d] Yes. 53. 9
v. 31
[e] Sal. 69. 21
[f] Mat.27.48
[g] Mat. 28. 1
[h] Yoh. 17. 4
[i] Yoh. 19. 26
[j] Marko 15. 42
[k] Deut. 21. 23
[l] Luka 24. 12
[m] Yoh.19.40
[n] Yoh.11.44
[o] 1 Yoh. 5. 6, 8
[p] 1 Yoh. 1. 1-3
[r] Sal. 16. 10 Mac. 2. 25-31
[s] Eks.12.46
[t] Sal.22.16, 17 Zek.12.10
[u] Luka 24. 16-31 Yoh. 21. 4
[v] Mat. 27. 57, 58
[w] Yoh.3.1,2





nao, Cifukwa anacotsa Ambuye wa-
nga, ndipo sindidziwa kumene ana-
muika Iye. 14 M'mene adanena izi,
anaceuka m'mbuyo, naona Yesu ali
ciriri, ndipo [a] sanadziwa kuti ndiye
Yesu. 15 Yesu ananena naye, Mkazi,
uliranji? ufuna yani? Iyeyu poyesa
kuti ndiye wakumunda, ananena ndi
Iye, Mbuye ngati mwamnyamula Iye,
ndiuzeni kumene mwamuika Iye,
ndipo ndidzamcotsa. 16 Yesu ana-
nena naye, Mariya. Iyeyu m'mene
anaceuka, ananena ndi Iye m'Ci-
hebri, Raboni; cimene cinenedwa,
Mphunzitsi. 17 Yesu ananena naye,
Usandikhudze, pakuti sindinatha ku-
kwera kwa Atate; koma [e] pita kwa
abale anga, ukati kwa iwo, Ndikwera
kunka kwa Atate wanga, ndi Atate
wanu, ndi Mulungu wanga, ndi Mu-
lungu wanu. 18 [g] Mariya wa Maga-
dala anapita, nalalikira kwa akuphu-
nzirawo, kuti, Ndaona Ambuye; ndi
kuti ananena izi kwa iye.

*Yesu aonekera kwa akuphunzira, Tomasi palibe.*

19 [i] Pamenepo, pokhala madzulo,
tsiku lomwelo, loyamba la Sabata,
makomo ali citsekere, kumene ana-
khala akuphunzira, cifukwa ca kuopa
Ayuda, Yesu anadza naimirira pakati
pao, nanena nao, Mtendere ukhale
ndi inu. 20 Ndipo pamene adanena
ici, anaonetsa iwo manja ace ndi nthiti
zace. [l] Pamenepo akuphunzira ana-
kondwera pakuona Ambuye. 21 Ci-
fukwa cace Yesu anatinso kwa iwo,
[m] Mtendere ukhale ndi inu; [n] monga
Atate wanditumu Ine, Inenso nditumu
inu. 22 Ndipo pamene anati ici ana-
wapumira, nanena nao, Landirani
Mzimu Woyera. 23 [p] Zocimwa za
anthu ali onse muwakhulukira, zikhu-
lulukidwa kwa iwo; za iwo amene
muzigwiritsa, zagwiritsidwa.
24 Koma [t] Tomasi, mmodzi wa
khumi ndi awiriwo, wochedwa Di-
dimo, sanakhala nao pamodzi, pa-
mene Yesu anadza. 25 Cifukwa cace
akuphunzira ena ananena naye, Ta-
muona Ambuye. Koma iye anati
kwa iwo, Ndikapanda kuona m'manja
ace cizindikilo ca misomaliyo, ndi
kuika cala canga m'cizindikilo ca
misomaliyo, ndi kuika dzanja langa
ku nthiti yace; sindidzakhulupira.

*Yesu aonekera kwa akuphunzira, Tomasi ali nao.*

26 Ndipo pakupita masiku asanu
ndi atatu akuphunzira ace analinso
m'nyumbamo, ndi Tomasi pamodzi
nao. Yesu anadza, makomo ali
citsekere, naimirira pakati, nati,
Mtendere ukhale ndi inu. 27 Pomwe-
po ananena kwa Tomasi, [b] Bwera naco
cala cako kuno, nuone manja anga;
ndipo bwera nalo dzanja lako, nuliike
ku nthiti yanga, ndipo usakhale
wosakhulupira, koma wokhulupira.
28 Tomasi anayankha nati kwa Iye,
Ambuye wanga, ndi Mulungu wanga.
29 Yesu ananena kwa iye, Cifukwa
wandiona Ine, wakhulupira; [c] odala
iwo akukhulupira, angakhale sanaona.
30 Ndipo [d] zizindikilo zina zambiri
Yesu anazicita pamaso pa akuphu-
nzira ace, zimene sizinalembedwa
m'buku ili; 31 koma [f] zalembedwa
izi kuti mukakhulupirire kuti Yesu
ndiye Kristu Mwana wa Mulungu, ndi
kuti [h] pakukhulupira mukhale nao
moyo m'dzina lace.

## 21 *Yesu awaonekera ku Nyanja ya Tiberiya.*

Zitapita izi Yesu anadzionetseranso
kwa akuphunzira ace ku nyanja ya
Tiberiya. Koma anadzionetsera co-
tere.
2 Anali pamodzi Simoni Petro, ndi
Tomasi, wochedwa Didimo, ndi [j] Nata-
nayeli wa ku Kana wa ku Galileya,
ndi [k] ana a Zebedayo, ndi awiri ena a
akuphunzira ace. 3 Simoni Petro
ananena nao, Ndinka kukasodza.
Ananena naye, Ifenso tipita nawe.
Anaturuka, nalowa m'ngalawa; ndi-
po m'usiku muja sanagwira kanthu.
4 Koma pakuyamba kuca Yesu
anaimirira pambali pa nyanja, ko-
matu akuphunzirawo [o] sanadziwa kuti
ndiye Yesu. 5 Yesu ananena nao,
[r] Ananu, muli nako kanthu kakudya
kodi? Anamyankha Iye, Iai. 6 Ko-
ma anati kwa iwo, [s] Ponyani khoka
ku mbali ya dzanja lamanja ya nga-
lawa, ndipo mudzapeza. Pamenepo
anaponya, ndipo analibenso mphamvu
yakulikoka cifukwa ca kucuruka
nsomba. 7 Pamenepo [u] wophunzira
uja amene Yesu anamkonda ananena
kwa Petro, Ndiye Ambuye. Simoni
Petro pakumva kuti ndiye Ambuye,
anadzibveka maraya a pathupi pakuti
anali wamarisece, nadziponya yekha
m'nyanja. 8 Koma akuphunzira ena
anadza m'kangalawa, pakuti sanali
kutali ndi mtunda, koma monga
mikono mazana awiri, nakoka khoka
la nsombazo. 9 Ndipo pamene ana-
turukira pamtunda, anapenya moto
wamakara pomwepo, ndi kansomba
kosanjikikako, ndi mkate. 10 Yesu

[a] Luka 24, 16-31 Yoh. 21. 4
[b] 1 Yoh. 1. 1
[c] 2 Akor. 5. 7
[d] Yoh. 21. 25
[e] Mat.28.10 Yoh. 16. 28
[f] Luka 1. 4
[g] Mat.28.10 Yoh. 16. 28
[h] Yoh. 3. 15, 16 1 Petr. 1. 8, 9
[i] Marko 16. 14 1 Akor. 15. 5
[j] Yoh. 1. 45
[k] Mat. 4. 21
[l] Yoh. 16. 22
[m] v. 19, 26
[n] Mat.28.18 Yoh. 17. 18
[o] Yoh. 20. 14
[p] Mat.16.19 „ 18.18
[r] Luka 24. 41
[s] Luka 5. 4, 6, 7
[t] Yoh. 11. 16
[u] Yoh. 13. 23

ananena nao, Tenganiko nsomba
zimene mwazigwira tsopano. 11 Ci-
fukwa cace Simoni Petro anakwera
m'ngalawa nakokera khoka kumtu-
nda lodzala ndi nsomba zazikuru, zana
limodzi, ndi makumi asanu ndi zitatu;
ndipo zingakhale zinacuruka kotere,
khoka silinang'ambika. 12 Yesu ana-
nena nao, [b] Idzani mufisule. Koma
palibe mmodzi wa akuphunzira anatha
kumfunsa Iye, Ndinu yani? podziwa
kuti ndiye Ambuye. 13 Yesu anadza
natenga mkate napatsa iwo, momwe-
monso nsomba. 14 [d] Imeneyo ndi
nthawi yacitatu yakudzionetsera Yesu
kwa akuphunzira ace, m'mene atauka
kwa akufa.
15 Ndipo pamene atafisula Yesu
ananena kwa Simoni Petro, Simoni
mwana wa Yona, kodi undikonda ine
koposa awa? Ananena ndi Iye, Inde,
Ambuye; mudziwa kuti ndikuko-
ndani Inu. Ananena naye, Dyetsa
ana a nkhosa anga. 16 Ananena
nayenso kaciwiri, Simoni mwana wa
Yona, ukonda Ine kodi? Ananena
ndi Iye, Inde, Ambuye; mudziwa
kuti ndikukondani Inu. Ananena
naye, [f] Weta nkhosa zanga. 17 Ana-
nena naye kacitatu, Simoni mwana
wa Yona, kodi undikonda Ine? Petro
anamva cisoni kuti anati kwa iye
kacitatu, Kodi undikonda Ine? ndi-
po anati kwa iye, Ambuye, [i] mudziwa
Inu zonse; muzindikira kuti ndi-
kukondani Inu. Yesu ananena naye,
Dyetsa nkhosa zanga. 18 [k] Indetu,
indetu, ndinena ndi iwe, pamene una-
li mnyamata unadzimangira wekha
m'cuuno, ndipo unayenda kumene
unafuna; koma pamene udzaka-
lamba udzaturutsa manja ako, ndipo
adzakumanga wina, nadzakunyamula
kumene sufuna. 19 Koma ici ana-
nena ndi kuzindikiritsa [a] imfa imene
adzalemekeza nayo Mulungu. Ndipo
m'mene ananena ici, anati kwa iye,
Nditsate Ine. 20 Petro, m'mene ana-
ceuka, anapenya [c] wophunzira amene
Yesu anamkonda alikutsata, amene-
nso anatsamira pacifuwa pace pa-
mgonero, nati, Ambuye, ndani iye
wakupereka Inu? 21 Pamenepo Pe-
tro pakumuona, ananena kwa Yesu,
Ambuye, koma nanga uyu? 22 Yesu
ananena naye, Ngati ndifuna uyu
akhale [e] kufikira ndidza Ine, kuli
ciani ndi iwe? unditsate Ine iwe.
23 Cifukwa cace mau awa ana-
turuka kufikira kwa abale, kuti
wophunzira uyu sadzafa. Koma Ye-
su sananena kwa iye kuti sadzafa;
koma, Ngati ndifuna iye akhale ku-
fikira ndidza, kuli ciani ndi iwe?
24 Yemweyu ndiye wophunzira
wakucita umboni za izi, ndipo ana-
lembera izi; ndipo [g] tidziwa kuti
umboni wace ndi woona.
25 Koma [h] palinso zina zambiri zi-
mene Yesu anazicita, zoti zikada-
lembedwa zonse phe, [j] ndilingalira
kuti dziko lapansi silikadakhala nao
malo a mabuku amene akadalembe-
dwa. Amen.

[a] 2 Petr. 1. 14
[b] Mac. 10. 40, 41
[c] Yoh. 20. 2
[d] Yoh. 20. 19, 26
[e] Mat. 16. 27, 28
„ 25. 31
1 Akor. 4. 5
„ 11. 26
Cibv. 2. 25
„ 22. 7, 20
[f] Mac. 20. 28
[g] Yoh. 19. 35
[h] Yoh. 20. 30
[i] Yoh. 2. 24, 25
[j] Amos. 7. 10
[k] Yoh. 13. 36
Mac. 12. 3, 4

# MACITIDWE A ATUMWI

## 1 *Yesu akwera kunka Kumwamba.*

(Mat. 28. 19, 20. Marko 16. 19.
Luka 24. 51.)

TAONANI [b] Teofilo inu, mau aja
oyamba ndinakonza, za zonse Yesu
anayamba kuzicita ndi kuziphunzitsa,
2 [e] kufikira tsiku lija anatengedwa
kunka Kumwamba, [f] atatha kulamu-
lira mwa Mzimu Woyera atumwi
amene adawasankha; 3 kwa iwonso
anadzionetsera yekha wamoyo ndi
zitsimikizo zambiri, zitatha zowawa
zace, [i] naonekera kwa iwo masiku
makumi anai, ndi kunena zinthu za
Ufumu wa Mulungu; 4 ndipo [j] poso-
nkhana nao pamodzi, anawalamulira
asacoke ku Yerusalemu, komatu ali-
ndire lonjezano la Atate, limene, anati,
munalimva kwa Ine; 5 pakuti
Yohane anabatizadi ndi madzi; koma
[a] inu mudzabatizidwa ndi Mzimu
Woyera, asanapite masiku ambiri.
6 Pamenepo iwowa, atasonkhana
pamodzi, anamfunsa Iye, nanena,
Ambuye, [c] kodi nthawi yino mubwe-
zera ufumu kwa Israyeli? 7 Koma
anati kwa iwo, [d] Sikuli kwa inu ku-
dziwa nthawi kapena nyengo, zimene
Atate anaziika m'ulamuliro wace wa
Iye yekha. 8 Komatu [g] mudzala-
ndira mphamvu, Mzimu Woyera ata-
dza pa inu: ndipo [h] mudzakhala mboni
zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya
lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira
malekezero ace a dziko. 9 Ndipo
m'mene adanena izi, ali cipenyerere
iwo, ananyamulidwa; ndipo mtambo
unamlandira Iye kumcotsa kumaso
kwao. 10 Ndipo pakukhala iwo
cipenyerere kumwamba pomuka Iye,

[a] Yow. 2. 28
Mac. 2. 4
[b] Luka 1. 3
[c] Yes. 1. 26
[d] Mat. 24. 36
[e] Marko 16. 19
v. 9
[f] Mat. 28. 19
[g] Mac. 2. 1, 4
[h] Luka 24. 48
[i] Luka 24. 36
1 Akor. 15. 5-8
[j] Luka 24. 49





taonani, amuna awiri obvala zoyera
anaimirira pambali pao; 11 amene-
nso anati, [a] Amuna a ku Galileya,
muimiranji ndi kuyang'ana kumwa-
mba? Yesu amene, walandiridwa
kunka Kumwamba kucokera kwa
inu, [b] adzadza momwemo monga
munamuona alinkupita Kumwamba.
12 Pamenepo anabwera ku Yeru-
salemu kucokera ku phiri lonenedwa
la Azitona, limene liyandikana ndi
Yerusalemu, loyendako tsiku la Sa-
bata. 13 Ndipo pamene adalowa,
anakwera ku cipinda ca pamwa-
mba, kumene analikukhalako; ndiwo
[e] Petro ndi Yohane ndi Yakobo ndi
Andreya, Filipo ndi Tomasi, Barto-
lomeyu ndi Mateyu, Yakobo mwana
wa Alifeyu, ndi Simoni Zelote, ndi
Yuda mwana wa Yakobo. 14 [g] Iwo
onse analikukangalika m'kupe-
mphera, pamodzi ndi akazi, ndi
Mariya, amace wa Yesu, ndi abale
ace omwe.
15 Ndipo m'masiku awa anaimirira
Petro pakati pa abale, nati (gulu la
anthu losonkhana pamalo pomwe
ndilo ngati zana limodzi ndi makumi
awiri), 16 Amuna inu, abale, kuna-
yenera kuti lemba likwanitsidwe,
[j] limene Mzimu Woyera anayamba
kunena mwa m'kamwa mwa Davide
za Yudase, wokhala mtsogoleri wa
iwo adagwira Yesu. 17 Cifukwa
anali wowerengedwa mwa ife, ndipo
analandira gawo lace la utumiki uwu.
18 [l] (Uyutu tsono anadzitengera ka-
dziko ndi mphotho ya cosalungama;
ndipo anagwa camutu, naphulika pa-
kati, ndi matumbo ace onse anakhu-
thuka; 19 ndipo cinadziwika ndi
onse akukhala ku Yerusalemu; ko-
tero kuti m'manenedwe ao kadzi-
koka kanachedwa Akeldama, ndiko,
kadziko ka mwazi.) 20 Pakuti kwa-
lembedwa m'buku la Masalmo,

[m] Pogonera pace pakhale bwinja,
Ndipo pasakhale munthu wogo-
napo;
Ndipo uyang'aniro wace autenge
wina.

21 Potero kuyenera kuti wina wa
amunawo anatsatana nafe nthawi
yonseyi Ambuye Yesu analowa
naturuka mwa ife, 22 [n] kuyambira
ubatizo wa Yohane, kufikira tsiku
lija anatengedwa kunka Kumwamba
kutisiya ife, mmodzi wa awa akhale
mboni ya kuuka kwace pamodzi ndi
ife. 23 Ndipo anaimikapo awiri,
Yosefe wochedwa Barsaba, amene
anachedwanso Yusto, ndi Matiya.
24 Ndipo anapemphera, nati, [o] Inu,
Ambuye, wozindikira mitima ya onse,
sonyezani mwa awa awiri mmodziyo
amene munamsankha, 25 alowe malo
a utumiki uwu ndi utumwi, kuco-
kera komwe Yudase anapatukira,
kuti apite ku malo a iye yekha.
26 Ndipo anayesa maere pa iwo;
ndipo anagwera Matiya; ndipo ana-
werengedwa pamodzi ndi khumi ndi
mmodziwo.

## 2 *Tsiku la Pentekoste.*

Ndipo pakufika [c] tsiku la Pente-
koste, [d] anali onse pamodzi pa malo
amodzi. 2 Ndipo mwadzidzidzi ana-
mveka mau ocokera Kumwamba
ngati mkokomo wa mphepo yolimba,
[f] nadzaza nyumba yonse imene ana-
likukhalamo. 3 Ndipo anaonekera
kwa iwo malilime ogawanikana, onga
amoto; ndipo unakhala pa iwo onse
wayekha wayekha. 4 Ndipo [h] ana-
dzazidwa onse ndi Mzimu Woyera,
[i] nayamba kulankhula ndi malilime
ena, monga Mzimu anawalankhulitsa.
5 Koma anali m'Yerusalemu okha-
lako Ayuda, amuna opembedza, oco-
kera ku mtundu uli wonse pansi pa
thambo. 6 Koma pocitika mau awa,
unyinji wa anthu unasonkhana, nu-
sokonezedwa, popeza yense ana-
wamva alikulankhula m'cilankhu-
lidwe cace ca iye yekha. 7 Ndipo
anadabwa onse, nazizwa, nanena,
Taonani, [k] awa onse alankhulawa sali
Agalileya kodi? 8 ndipo nanga ife
timva bwanji, yense m'cilankhulidwe
cathu cimene tinabadwa naco?
9 Aparti ndi Amedi, ndi Aelami,
ndi iwo akukhala m'Mesopotamiya,
m'Yudeya, ndiponso m'Kapadokiya,
m'Ponto, ndi m'Asiya; 10 m'Frugiya,
ndiponso m'Pamfuliya, m'Aigupto,
ndi mbali za Libiya wa ku Kurene,
ndi alendo ocokera ku Roma, ndiwo
Ayuda, ndiponso opinduka, 11 Akrete,
ndi Aarabu, tiwamva iwo alikulankhu-
la m'malilime athu zazikuru za Mu-
lungu. 12 Ndipo anadabwa onse,
nathedwa nzeru, nanena wina ndi
mnzace, Kodi ici nciani? 13 koma
ena anawaseka, nanena kuti, Akhuta
vinyo walero.

### *Codzikanira ca Petro.*

14 Koma Petro, anaimirira pamodzi
ndi khumi ndi mmodziwo, nakweza
mau ace, nanena kwa iwo, nati,
Amuna inu Ayuda, ndi inu nonse
akukhala kwanu m'Yerusalemu, ici
cizindikirike kwa inu, ndipo cherani
khutu mau anga. 15 Pakuti awa
sanaledzera monga muyesa inu; pa-

[a] Mac. 2. 7
[b] Mat. 24. 30
[c] Lev. 23. 15
[d] Mac. 1. 14
[e] Mat. 10. 2-4
[f] Mac. 4. 31
[g] Mac. 2. 1, 46
[h] Mac. 1. 5
[i] Marko 16. 17
1 Akor. 12. 10, 28, 30
[j] Sal. 41. 9
[k] Mac. 1. 11
[l] Mat. 27. 5, 7, 8
[m] Sal. 69. 25
„ 109. 8
[n] Marko 1. 1-
[o] 1 Sam. 16. 7